


# KUPANGA NJIRA

 Madzulo abwino, abwenzi. Ndipo Ambuye akudalitseni inu mochuluka. Ndipo zikomo inu, M'bale Neville, chifukwa cha ndemanga yokoma imeneyo. Ndine wokondwa kwambiri kubwerera ku kachisi usikuuno, mu utumiki wa Ambuye wathu wodala, ndi kuwawona azimzathu kunjako, usikuuno, kuti adzamupembedze Iye ndi ife.

<sup>2</sup> Ndithudi ndi mwayi waukulu kukumana kenanso mbali ino Kudza kwa Ambuye. Ndipo titatha kuwona, kumva, ambiri akuchoka, mosayembekezereka, mofulumira kwambiri, ife timangodabwa, nthawi ndi nthawi, ndani ati atsatiye. Koma, pokhala nacho chitsimikiziro chodala ichi, kuti ngati . . . “palibe chimene chingatilekanitse ife ku chikondi cha Mulungu chimene chiri mwa Khristu. Palibe imfa, kapena—kapena palibe chirichonse pano, kapena chamtsogolo, kapena mphamvu zirizonse, zimene zingatilekanitse ife ndi chikondi cha Mulungu chimene chiri mwa Khristu Yesu.” Ndipo podziwa ichi, kuti, “Msasa wa pansi pano ukadzaphwasuka, ife tiri nawo wina ukudikirira.” Osakonzeka, osakhazikika; ndipo ife tikupuma pa chiyembekezo chodala chimenecho chaulemelero.

<sup>3</sup> Ine ndinali kuyankhula ndi mkazi wanga, ndi Akazi a Wood ndi iwo, basi . . . ine nditabwerera. Ine ndimati, “Chabwino, zikungowoneka ngati ndi ulendo pambuyo pa ulendo, ndi malo pambuyo pa malo, koma, komabe, iwo akumakhala a ulemerero mochuluka. Ndipo ine . . . podziwa kuti tikufika kotsekera, a—a—kuyandikira kwa Kudza kwa Ambuye.” Ine ndinati, “Chabwino . . .”

<sup>4</sup> Ndikuyankhula kwa mnyamata wanga, ndikubwera ndikutsika mu msewu tsiku lina, ndikuchokera ku Sioux Falls, South Dakota. Kenako ine ndinati, “Iwe ukudziwa, kunyumba ndi malo abwino kwambiri.” Ife tinali tikubwerera kunyumba. Ine ndinati, “Timakonda dziko lino. Kuno ndi kwathu. Ife tikhoza kusaganiza kuti ndi choncho, koma ndi choncho. Tinabadwira kwathu kuno. Ili, Mulungu anadziyiyika ife kuno. Ife tinalibe njira yodzibweretsera tokha kuno. Ngakhale abambo athu ndi amayi analibe njira iliyonse. Zimenezo zimayenera kukhala mmanja a Mulungu. Anthu ambiri ali pabanja, sanakhalepo ndi mwana. Koma, Mulungu anawona kuti ife tikanadzabwera pa dziko lapansi lino.

<sup>5</sup> Ndiyeno pamene ife tinabwera, ife tinayamba kumakula ndi kumawumbidwa kudzakhala thupi, mwa ma atomu ndi kuwala, ndi zina zotero, pamene ilo linayamba kutengera dziko lapansi. Ndipo kenako titafika pa usinkhu winawake, iwo

anasiya kukula. Ife timawawonjezerabe iwo kwa ife, koma iwo akuchokapo. Imfa yadzalowa.

<sup>6</sup> “Ndipo kenako pamene msasa wa pansi pano udzaphwasuka, ife tiri nawo wina ukuyembekezera kumeneko.” Mukuona? Ife tidzakalowa mmenemo, ife tidzadziwana wina ndi mzake. Ife sitingakhoze kugwirana chanza; sitidzakhala nako kumverera kwa kukhudza kumeneko. Ife sitingathe... Sindingathe kukugwirani chanza, kunena, “Muli bwanji, m’bale,” chifukwa ine—ine...inu simukakhala ndi dzanja la mtundu umenewo. Koma, komabe, ife sitiri mu thupi logwirika monga ife tiri tsopano, ife tiri mu a—thupi lakumwamba. Ndipo kenako pamene ili . . .

<sup>7</sup> Ndipo ine ndimaganiza, uko mu Igupto, kuti pamene Yosefe anasiya chikumbutso, kwa ana a Israeli, mafupa ake, kuti tsiku lina iwo adzatuluka. Ndipo pamene iwo azidzatuluka, iwo akanadzatenga mafupa ake ndi iwo, kupita ku dziko lolonjezedwa. Ndipo Mhebri aliyense amene anakhumba kuti abwerere ku dziko lakwawo, chotero ziribe kanthu momwe iye ankakhalira bwino, komabe chikhumbo chake chinali kubwerera kwawo. Ndipo nthawi iliyonse iwo akamadutsa ndi kuwona mafupa amenewo, iwo ankadziwa kuti tsiku lina iwo adzabwerera ku dziko la kwawo.

<sup>8</sup> Pamene ife tiri kuno, tikuyembekezera kuti tiwoloke kuchoka pa malo ano, ife tikuwona manda apululu kutsidya uko mu Yerusalemu, akutidziwitsa ife kuti chinachake chinachitika. Ndiyeno pamene ife tidzavala la ulemelero ilo...osati la ulemelero, koma thupi lakumwamba, ndipo ife nkumayendayenda mu maiko a Ulemelero ndi Khristu, kumayang’anana pa wina ndi mzake, kumayankhulana kwa wina ndi mzake; tikhoza kuyankhula. Miyoyo pansi pa guwa, ikulira, “Mpaka liti?” Ndiyeno nchiyani chidzakhale chikumbutso kumeneko, kuti ife tikubwereranso ku dziko lapansi kudzadya ndi kumwa ndi kugona? Apo Iye adzakhala ali, atakhala pamenepo pa Mpandowachifumu, mu thupi logwirika. Amen.

<sup>9</sup> Tsiku lina Iye adzauka, mu thupi logwirika limenero. Ndipo pamene Iye azidzabwereranso, matupi ammwamba awa adzavala ulemelero. Kenako ife tidzakakhala monga Iye, ndipo tidzakakhala moyo kwanthawizonse mu thupi limenero. Chiyani... Chiyani—nchiyanso chiri chofunikira? Mukuona? Izo zakhazikika kale. Ndizo basi...Kungozikika pomwe apo. Ndipo kulola ichi . . .

Ziyembekezo zanga sizinamangidwe pa  
chirichonse  
Kuposa Magazi a Yesu ndi chirungamo;

Pamene zonse mozungulira moyo wanga  
zichoka,  
Ndiye iye ndi chiyembekezo changa chonse ndi  
pokhalapo.

<sup>10</sup> Khristu ndi Iye amene anapanga izo kukhala zotheka; osati mpingo wanga, kapena osati chipembedzo changa, osati azimzanga, koma Khristu.

Maziko ena onse ndi mchenga wotitimira,  
maziko ena onse.

<sup>11</sup> Nzosadabwitsa Eddie Perronet. . . Iwo ankaganiza kuti iye anali wopenga. Ndipo tsiku limenero, atakhala mmenemo ngati kapolo kwa anthu, Mzimu Woyera unamufikira ndipo anatola cholemba ndi kuyamba kulemba nyimbo yodabwitsa ija imene idzayimbidwe pa msonkhano wa mwambo wapamwamba wa kukhazikitsidwa kwa Mfumu ya mafumu: *Nonse Tamandani Mphamvu ya Dzina la Yesu.*

<sup>12</sup> Lipoti lodabwitsa lochokera kumtunda kumpoto tsopano. Ife tinali ndi azitumiki, osati azitumiki, koma kadzutsa wa a Christian Business Men ku . . . kumtunda ku Minneapolis, ndipo kadzutsa wamkulu amene ife tinayamba takhalapo naye wa amuna amalonda. Thuu sauzande anatulukira.

<sup>13</sup> Ndipo Ambuye anatipatsa ife Uthenga. Ndipo mmawa umenewo, mu kuyitanira paguwa, amuna amalonda fifite anabwera kwa Khristu ndipo anabadwa mwatsopano, mmawa umenewo mu msonkhano. Oh, izo zinangokondoweza mtima wanga, mwamuna wamalonda kubwera! Misonkhano yodabwitsa, kulikonse. Ambuye alemekezeke, ndipo ulemelero wonse kwa Iye!

<sup>14</sup> Ndipo tsopano ndiri ndi cholemba chaching'ono apa, chikuti, "Kodi ndikakhalako liti ku Indianapolis?" Pa Juni 11 mpaka 15, ndidzakhala ku Cadle Tabernacle ku Indianapolis, Indiana, June 11 kudutsa 15, kudzakhala anthu leveni sauzande.

<sup>15</sup> Likadutsa tsiku la mawa, ife tinyamuka kupita ku Shreveport, Louisiana, ndi kukakhala kumeneko kudutsa kumapeto kwa sabata ku Shreveport, Louisiana.

<sup>16</sup> Ndipo kenako ife tidzachoka ku Shreveport ndi kupita ku Houston, Texas, ndipo tidzakakhala kumeneko masiku awiri, limene lidzakhale Lolemba ndi Lachiwiri.

<sup>17</sup> Ndipo kenako pa 16 ife tidzakayambira mu Mexico wakale, Mexico City, Mexico wakale. Bambo Arganbright angondiimbira kumene ine. Ndipo iwo apezwa bwalo lalikulu la ng'ombe kumeneko, limene mumakhala anthu sikisite sauzande. Ndipo kuli matchalitchi foro handiredere akugwirizana, alembedwa kale. Ife tikuyembekeza handiredere sauzande ku msonkhanoko.

<sup>18</sup> Ndipo ndi nthawi yoyamba iyi. . .Ife tiri ndi chinachake choti timutamandire Mulungu. Nthawi yoyamba mu mbiri ya Mexico, imene boma linavomerezapo a Chiprotestanti kulowa ndi kutipatsa ife malo kuti tibwere. Nthawi yoyamba mu mbiri ya Mexico, a—imene Achiprotestanti analandiridwapo. Ndipo General Valdivia uja, ndi Mkulu wa asirikali a ku Mexico, wangobadwa mwatsopano kumene ndipo analandira Mzimu Woyera. Ndipo mwaulemu wake kwa bwanamkubwa wa Mexico, watipatsa ife ufulu wa boma kuti tilowe ndi chitetezo cha asirikali. Ndipo kuti ndife. . .

<sup>19</sup> Ine ndapeza bwalo lalikulu la ng'ombe. Ndicho chinthu chachikulu chimene chiripo mu Mexico yense. Mumakhala anthu sikisite sauzande, kuzungulira monga chonchi, pambali pa—chipinda chimene iwo amachitiramo zomenyana, inu mukudziwa, mmenemo. Ndipo ife tikakhala nalo kwa mausiku teni otsogozana tsopano, popanda kusokonezedwa kulikonse, molunjika kwa mausiku teni otsogozana. Mukhale mukundipempherera ine.

<sup>20</sup> Ine ndikungomverera. . .ndikumva phokoso la mvula yambiri kumusi uko. Ine basi. . . Anthu a ku Mexico ndi ophweka kwambiri, okhulupirira odzichepetsa. Ndipo akangokhutitsidwa kamodzi. . .Iwo ndi Akatolika. Ndipo akangokhutitsidwa kamodzi kuti Choonadi ndi choonadi, ndiye izo zimakhazikitsa izo kwa onse.

<sup>21</sup> Ndiye, ndidzafulumira kubwerera kuchokera ku Mexico wakale, kudzabwerera kuno cha mma 30.

<sup>22</sup> Ndipo pa 1, uwo ndi mmawa wa Isitara, ku kachisi kuno, kwa msonkhano wa kutuluka kwa dzuwa. Ndipo msonkhano wa machiritso, udzatsatira iyo. Ndi utumiki wa ubatizo usiku umenewo, ku kachisi. Ndipo inu mukhoza kuwauza azimzanu, tsopano, kuti adzabweretse odwala awo onse ndi osautsika, ku msonkhano wa Isitara. Msonkhano wa kutuluka kwa dzuwa mmawa umenewo. Kenako, kutsatira iwo, mpaka teni koloko, hafu-naini nthawi ya Sande sukulu yokhazikika. Inu nonse mukonzekere zimenezo, Sande sukulu. Ndi a—msonkhano wa machiritso udzatsatira zimenezo, a-. . . msonkhano wa machiritso wachizolowezi monga ife timakhala nawo mmisonkhano yokopa anthu.

<sup>23</sup> Ndipo chotero, ndiye, Mexico City ikakhala nthawi yoyamba imene masomphenya atsopano awa, amene Ambuye andiuzwa ine, akakhale akugwira ntchito pa nthawi imeneyo. Chotero ife tidzayesera izo kenanso, Ambuye akalola, komwe kuno, Lamlungu la Isitara mmawa, pogwiritsa ntchito zipinda ziwiri izi, . . .?. . .apa, mwaona. Chotero ife tikuyembekezera nthawi yopambana kuno, mmawa wa Isitara.

<sup>24</sup> Ndipo umboni wakuti Ambuye Yesu wauka kwa akufa, Iye ndi wamoyo. Inde, bwana. Ndipo Iye wakhala ali wamoyo

kuyambira Isitala yoyamba ija. Ndipo Iye ali pano ndi ife ngakhale tsopano. Ndipo ine ndikungodalira kuti Ambuye atipatsa ife kutsanulidwa kwakukulu kwa madalitso Ake kwa mmawa umenewo.

<sup>25</sup> Kenako tidzapita ku...kuchokera ku, kuno kenako, ife tidzapita ku Chicago, pa 11, pa 3 mpaka pa 11. Ndipo ife tidzanyamuka Lolemba, kukayambira kumeneko Lachiwiri, ndi kuyambira kudutsa...Ayi, ndi pa 3 mpaka pa 8. Ndiyeno pa 11 tikayamba ku Charlotte...Ayi, Columbia, North Carolina. Ndipo kenako ku Spindale, North Carolina. Ndipo kenako, kuchokera kumeneko, tidzapita ku Charlotte, South Carolina. Ndipo kenako Anchorage, Alaska, kuchokera kumeneko; mpaka ku Anchorage, Alaska. Kenako, tidzabwerera. Ndipo sindinatsimikize, koma, mwina, mwinamwake pa nthawi imeneyo, chihema chidzakhala chiripo kuti tidzakhale pa msewu. Oh, ine basi...

<sup>26</sup> Inu mukudziwa chimene ine ndikufuna kuti ndichite? Kodi mungapemphere ndi ine pa ichi? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Penyani, Ine ndikufuna kuteru, nthawi isanapite, Ambuye akalola, kudzayika hema ameneyo komwe kuno mu Fall City uyu, ndi kukakhala kumeneko kwa msonkhano wa masabata foro kapena sikisi; kudzangokhala komwe kuno mpaka nkondo itatha. Ndipo inu mukhale mukupempherera zimenezo tsopano. Ndipo ine ndikufuna ndidzangoyika iyo kuno pakati pa Jeffersonville ndi New Albany kwinakwake, ndi kudzangoyika pafupifupi malo okhalamo seveni kapena eyiti sauzande mmenemo. Ndipo kenako ife tikhoza kudzawonjezera ana pamene masiku akupita, ndi kudzangokhala pomwe pano mpaka zitadzakhazikika. Amen.

<sup>27</sup> Ndiyeno, kenako, ine ndikuganiza ndiye pa 11 mpaka pa 15 Juni, ku Cadle Tabernacle mu Indianapolis. Ndipo kenako, pa 17, ine ndikukhulupirira, kudutsa 21 Juni, ndi ku Minneapolis, mu bwalo la mpira kunja uko, kokhala twente-seveni sauzande. Umenewo ndi msonkhano waukulu wa Christian Business Men, kuyankhula, ndi kukhala ndi kupempherera odwala usiku uliwonse.

<sup>28</sup> Ndipo tsopano muzipempherera izi, muzichita, ndi kupempherera molimba. Ine—ine ndikungomverera kuti tiribe nthawi yochuluka tsopano. Ndipo ine ndikuneneratu izo; ine sindikunena kuti awa ndi Ambuye akunena izi tsopano. Ine—ine ndikuneneratu kuti chaka chino Amerika alandira Khristu kapena amukana Khristu. Mukuona? Ine ndikukhulupirira kuti iyi ikhala nthawi yotembenukira, imene Amerika adzalowemo. Ife tidzakhala ndi chitsitsimutso mu tsiku ili, kapena ife sitidzakhala ndi chitsitsimutso. Ndipo ndikukhulupirira kuti ichi ndi chaka chimene Amerika adzapange chisankho chake. Ndipo ine ndikudalira kuti iwo adzapanga zimenezo ndipo ife tidzakhala ndi chitsitsimutso chachikulu chimene chiti

chidzangosesa. Ife tiri ndi kulalikira kochuluka, ndi uvangeri wochuluka, koma ife tikusowa chitsitsimutso (sichoncho ife?), chitsitsimutso chenicheni. Ndi chimene ife tikuchisowa. Ambuye akudalitseni inu.

<sup>29</sup> Wokondwa kumuwona M'bale Graham apo, ndi—ndi ine—ine ndikukhulupirira M'bale Smith wakhala patsogolo pa iye, M'bale Smith wochokera ku mpingo wa Mulungu. Ndipo—ndipo muli atumiki angapo muno, ine ndikutsimikiza. Ndipo ife tikukulandirani inu nonse, abale, wina aliyense, ndi alendo pa zipata zathu, ndi osonkhana onse. Ife timangokukondani inu.

<sup>30</sup> Ndipo tsopano ndi zolengeza izi, ndi kuzindikira kuti usikuuno, usiku wa mgonero wa utumiki wa mgonero. Ndipo zimupemphererani zolimba M'bale wathu wokonedwa Neville amene wagwira linga kuno ku kachisi, akuchita ntchito yaikulu; ndi kwa oyera onse kulikonse. Oh, ndi nthawi yosowa bwanji! Ndi nthawi yosowa bwanji! Ine ndikuzimva izo kuchokera uko ku Afrika, ndi kuyitana koteroko kwa ku Afrika.

<sup>31</sup> Ndipo M'bale Arganbright amangondiuzwa ine pa foni, kanthawi kapitako, kuti mfumu ya—ya ena mwa mayiko awo kumusi uko, ine ndaiwala kumene iko kunali, ine ndikukhulupirira kuno ku Sweden, Switzerland. Ine ndizipeza izo mu miniti. Denmark, wa—walemba kalata yapadera kupanga nyengo ino kuti ndipite kumeneko panthawi ino.

Mu Afrika ndi India, malo osiyanasiyana!

<sup>32</sup> Kumene, Zilumba za Hawaii zinalowako tsiku lina. Ndi pafupifupi ka teni molunjika kamene iwo ayitanira chitsitsimutso. A Christian Business Men akufuna kupita kunja uko ndi kungowulukira pamenepo, kukapanga dongosolo, kukakonza chaputala ndi kukawayankhulira iwo mmawa umenewo, ndipo kenako nkukayamba chitsitsimutso mu Hawaii.

<sup>33</sup> Chotero, dziko lonse lakhala parishi yathu, mwaona, dziko lonse. Ndipo ife ndi antchito Ake.

<sup>34</sup> Chotero tiyeni ife tizikumbukira, abwenzi, kuti uno ukhoza kukhala usiku wotsiriza, ichi chikhoza kukhala chaka chotsiriza, kapena ukhoza kukhala m'badwo wotsiriza. Mukuona? Ife sitikudziwa. Koma, mulimonse, ife tikudziwa ichi choona, kuti amoyo amadziwa kuti adzayenera kufa. “Kunaikidwa kamodzi kwa munthu ku imfa, ndipo pambuyo pake Chiweruzo.” Ndipo ngati alipo aliyense pano usikuuno, amene sanakonzeka kuti akomane ndi zimenezu, ndipo alibe chiyembekezo chodala ichi, mulole uno ukhale usiku umene inu muti mupange chiganizo cha Ambuye Yesu, kwa kamodzi, kwa Muyaya.

Tsopano tiyeni tipemphere.

<sup>35</sup> Atate athu Akumwamba, ife tikufuna kuti tikuthokozeni Inu kuchokera mu kuya komwe kwa mitima yathu, podziwa kuti ife tikuyembekezera kuno, osati okhumudwa konse; ziribe kanthu iwo apanga mabomba a atomiki ochuluka bwanji, ndi anthu ogwira ntchito za boma ochuluka bwanji amene iwo angawayike kuti aziyang'anira ndege, dziko likunjenjemera ndi kugwedezeke. Ife tikutsamira pa chiyembekezo chodala ichi chimene tiri nacho. Ife tikudalira mu ntchito yotsirizidwa ya Mulungu pa Kalvare, kudzera mwa Khristu. Podziwa ichi, kuti msasa wa pansu pano ukadzaphwasuka, ife tiri nawo wina ukuyembekezera kutsidya; waulemelero mochuluka, wochuluka kwambiri, kumene kulibe zowawa kapena kuzunzika, matenda. Kulibe ukalamba umene udzakanthe iwo, kopanda imvi, kopanda makwinya, koma ife tidzakakhala achichepere kumeneko kwanthawizonse.

<sup>36</sup> Baibulo lodalitsidwa, limene silinganene chirichonse koma choonadi, latipatsa ife chitsimikizo chodala ichi. Ndipo Mzimu Woyera, nawonso, ndi mboni, ukuchitira umboni za chomwecho. Mitima yathu ikulakalaka zimenezo. Ndipo ife tikudziwa kuti Baibulo limatiuza ife choncho, amene ali Mawu a Mulungu, mbewu zobzalidwa pa nthaka yachonde iyi kuti tipume mu chiyembekezo ichi.

<sup>37</sup> Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu mukhudze munthu aliyense usikuuno, kunja kwa Khristu. Ndi kuwabweretsa iwo pafupi apa, kuyenda kodabwitsa. Chiritsani odwala amene akhala pano usikuuno, Ambuye. Mosakayikira, mwa anthu ambiri awa, pakuyenera kukhala matenda pakati pathu. Ndipo ife tikupemphera kuti Inu muchize aliyense.

<sup>38</sup> Tsopano mubwere ku Mawu, Atate. Mutenge Mawu amene ali mzere wa moyo. Mizu, Ambuye, ya chitukuko chonse. Ife tikupemphera kuti Mzimu Woyera utenge Mawu aliwonse ndi kuwapereka Iwo ku mtima monga momwe ife tikusowera. Mulole ife tiyanjane mozungulira Mawu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

<sup>39</sup> Kwa kuwerenga pang'ono kwa Malemba, usikuuno, kwa basi—mutu waung'ono, kuti tiyesere kupeza zoyankhula, ndi kukhala mofulumira ku Mawu, kuti ife tikhoze kukhala ndi mgonero. Mawa pokhala Lolemba, ine ndikudziwa kuti ife sitikonda kuganiza za zinthu zimenezo, za kubwerera ku ntchito, koma ife tikuyenera kukumana nazo izo. Ndipo nthawi zambiri, inu mukudziwa...Koma, kuwonjezera apo, izi ndi zofunikira kwambiri kuposa ntchito ndi china chirichonse. Mukuona? Pakuti, ntchito yanu idzatha, tsiku lina, ndipo inu mudzatha ndi iyo. Koma ngati inu muli ndi Moyo Wamuyaya, inu simudzakhala nawo konse mathero. Ndi Wamuyaya; kukhala moyo, womangopitirira. Taganizani za zimenezo. Moyo womangopitirira, wopanda mathero. Pamene nusu za nthawi zapita, inu mudzakhalapobe kumeneko. Pamene mamilioni a

zaka adutsa, ife tidzakhala tiripobe kumeneko. Chotero, kwa masiku pang'ono chabe kuno padziko lapansi, ntchito sizichita mochuluka. Basi kungotithandizira ife, kugula zakudya zathu zapang'ono, ndi zina zotero, kudya, zomwe ife tikuyenera kuti tikhale nazo.

<sup>40</sup> Tsopano mu Akorinto Woyamba mutu wa 10, kuyambira ndi ndime ya 12.

Chifukwa chake *muloleni iye amene akuganiza kuti wayima ayang'ane kuwopa kuti iye angagwe.*

*Apo sipanakhalepo yesero linakutengani inu koma zotere...ndi zodziwika kwa munthu: koma Mulungu ndi wokhulupirika, amene sali...amene—amene akufuna kuti inu...sakufuna kuti inu muyesedwe koposa icho chimene inu mungakwanitse; koma...ndi yesero lirilonse adzapanga njira yothawirapo, kuti ife tithe kupirira ilo.*

<sup>41</sup> Ndi ndime yokongola bwanji! Ambuye awonjezere madalitso Ake kwa iyo. *Kupanga Njira*, chingakhale chimene ine ndikufuna kuti ndiyankhulepo, usikuuno. Kudziwa...Mulole Iye awonjezere madalitso Ake ku Mawu Ake, pamene ife tikumvetsera tsopano ku Mawu.

<sup>42</sup> Ndi lingaliro langa, kuti ngati Mawu, amene ali mizu, amene ali chinthu chimene chimagwira. Nthawi zambiri mu misonkhano yanga ya machiritso, ine—ine ndimayesetsa kuti, ngakhale aphunzitsi atadutsa kale zonsezo, Ine ndimayesetsa kuti ndibwerere ndi—ndi kudzatenga Mawu ndi kudzayika maziko.

<sup>43</sup> Mausiku angapo apitawo, ine ndinalandira kalata yaying'ono yonditsutsa, chimene zinali zabwino. Munthu anandiuzwa ine, anati, “M'bale Branham, inu ndi mnyamata chabe, apobe.” Anati, “Ine ndinali ndikulalikira Uthenga inu musanabadwe.” Ndipo iye anati, “Ine...Zaka zanga zonse forte-sikisi, komabe...” Iye—iye anali mphunzitsi wa sukulu ina ya Baibulo. Iye anati, “Koma munthu, wa mtundu wanu, amene amaphunzitsa anthu, ndipo komabe nkukhoza kupanga ndemanga imene inu munapanga usiku wina.” Anati, “Ndikuganiza kuti ndi zopusa.” Anati, “Inu munanena kuti mdierekezi analibe mphamvu yochiritsa.” Iye anati, “Mwinamwake, bwanji ngati ine nditakuuzani inu kuti mdierekezi ali ndi mphamvu yochiritsa.” Anati, “Tsopano inu mukandifunsa ine, ngati inu mukanimapo, chifukwa chimene ine ndikudziwa.” Anati, “Ine ndikuuzani inu.” Anati, “Mu tawuni yathu, muli mkazi amene amakhala kumeneko amene ali ndi a—mzimu woyipa. Ndipo iye...Anthu amabwera kwa iye kuti adzachiritsidwe.” Akuti, “Iye amamwetula tsitsi pamutu pawo, ndipo amapopa magari kuchokera mmitsempha mwawo, ndi kuwakulunga iwo mu tsitsi ili. Kuyenda kupita



ku mtsinje, ndi kuponyera chinthu ichi pa phewa lake, ndipo osayang'ana mmbuyo. Ngati iye ayang'ana mmbuyo," anati, "ndiye nthendayo imakhalabe ndi munthuyo. Koma iye amayenera kuti akaiponyere iyo mu mtsinje, ngati kunali kuyiwala, ndi kuchokapo." Ndipo anati, "Sikisite peresenti ya anthu, ife tinkawerengera, amachiritsidwa." Anati, "Tsopano, ngati mdierekezi sangathe kuchiritsa, nanga bwanji zimenezo?"

<sup>44</sup> Chotero, ine ndinadzamuyankha iye. Ine ndinati, "M'bale wanga wokoma mtima, wokonedwa, ndi kulemekeza konse ku zaka zanu," mwaona, "kulemekeza konse ku zaka zanu za kuphunzitsa, koma ine ndikuuzani inu tsopano kuti Yesu Khristu ananena kuti mdierekezi alibe mphamvu yochiritsa. Ndipo ngati Yesu ananena zimenezo, izo ndi zokhazikika, ndi ine. Iye anati, 'Ngati Satana atulutsa Satana, ndiye kuti ufumu wake wagawanika ndipo uli ndi mapeto. Ndipo iye sangatulutse Satana.' Ndiye inu mukhoza kundifunsa ine, 'Nchifukwa chiyani anthu awa amachiritsidwa?' Bwanji, si munthuyo. Mfitiyo inalibe kanthu kochita ndi izo, osati kuposa momwe ine ndikanachitira ndi izo, kapena munthu wina aliyense. Ndi anthu amene akufikirakowo, akumaganiza kuti iwo akubwera njira yoperekedwa ndi Mulungu ya machiritso awo. Ndi chikhulupiriro chawo cha pawokha mwa Mulungu, chimene chikuchita kuchiritsako. Mukuona? Ndi mafikiridwe amene iwo akuganiza. Si mfitiyo, komanso sangakhale mwamunayo." Eya.

<sup>45</sup> Chotero, chomwecho, Uthenga ukhoza kungoyenda, kapena ukhoza kufikira monga momwe Mawu a Mulungu akuphunzitsidwira. Ndipo anthu amakhazikitsa ziyembekezo zawo pa Mawu Amuyaya a Mulungu. "Chikhulupiriro chimadza pakumva, kumva ndi Mawu."

<sup>46</sup> Dr. Adair, kuno mu mzinda, mzanga wokonedwa, ananena kwa ine tsiku lina, iye anati, "Billy, kodi iwe sukuganiza kuti ngati anthu atakhala ndi chikhulupiriro chogwira mtengo kunja uko, iwo angakhale ndi zotsatira zomwezo?"

<sup>47</sup> Ine ndinati, "Kodi iwe ungakhale bwanji ndi chikhulupiriro mu zimenezo? Ngati iwe ungakhale ndi kuchuluka komweko kwa chikhulupiriro, kukhulupirira...kukhulupirira kuti iyo inali njira yoperekedwa ndi Mulungu, kuti iwe ugwire mtengowo, ndipo iwo ungachite izo, ndiye iwo akhoza kuchita zimenezo. Koma ndani ali ndi chikhulupiriro mu mtengowo?"

<sup>48</sup> Ine ndimakhala ndi chikhulupiriro mu zimene Mulungu ananena, ndipo ine ndimangotenga zimenezo. Chotero chikhulupiriro sichimamangidwa pa mchenga wotitimira wa—wa maganizo otengeka. Koma chikhulupiriro chimamangidwa pa muyezo, Mawu Amuyaya a Mulungu, Thanthwe la mibadwo. Apo ndi pamene chikhulupiriro chimatenga malo ake opumulirapo ndipo osasunthaponso, pamene icho chimangidwa pamenepepo.

<sup>49</sup> Tsopano, kupanga njira. Ine sindikhulupirira kuti Mulungu amayendetsa konse udindo Wake mwachisawawa. Ine—ine sindingayendetse wanga, inu simungayendetse wanu. Yesu sanafe pa Kalvare kuti adzangoti, “Chabwino, tsopano mwinamwake anthu andimvera ine chisoni, popeza kuti Ine ndabwera, kupita pa dziko lapansi ndi kudzatenga mawonekedwe a thupi. Ndipo iwo ndithudi adzapulumutsidwa, mwinamwake, ngati iwo adzawone momwe ine nditafere momvetsa chisoni.” Mulungu sanachite zimenezo. Yesu anafera cholinga chimodzi, ndipo icho chinali kudzapulumutsa iwo amene Mulungu anawadziwiratu kuti adzapulumutsidwa. Uko nkulondola. Mulungu ankadziwa kuti padzakhala winawake wopulumutsidwa, ndipo pankayenera kukhala kukonzekera, kapena njira yopangidwa kuti iwo adzapulumutsidwe. Ngati zikanapanda kutero, chipulumutso sichikanatheka.

<sup>50</sup> Chotero, Mulungu, podziwiratu kuti anthu akanadzapulumutsidwa, podziwa chimene iwo anali, Iye anachita kukonza dongosolo. Tsopano inu munganene kwa ine, “M’bale Branham, ndiye Mulungu amadziwa ndendende amene ati adzapulumutsidwe?” Kulondola. “Chabwino, nchifukwa chiyani Iwo amati, ‘Iye sakufuna kuti aliyense adzawonongeke?’” Iye satero. Iye safuna kuti aliyense adawonongeke, koma kuti onse adzafike ku kulapa.

<sup>51</sup> Koma, kuti akhale Mulungu, Iye akuyenera kudziwa amene ati adzachite izo, kapena Iye sanali Mulungu. Chifukwa, Iye ndi—Iye ndi wamphamvuzonse. Iye ndi wopezekapaliponse. Iye ndi wodziwazonse. Iye amadziwa chirichonse. Iye amakhala pamalo aliwonse, ndipo wamphamvuzonse. Chotero, kudziwiratu kumayang’ana mmbuyo ndi kunena kuti Iye anawoneratu izi, ndipo anadziwa, ndi chifukwa chake Iye amatha kudziwa chimene mapeto anali, kuchokera pachiyambi.

<sup>52</sup> Ndipo, chotero, podziwa kuti masiku onse odabwitsa awa amene ife tikukhalamo tsopano, ndi kuyima ndi kuchitira umboni, ndi kuwona zinthu zimene ife tikuziwona tsopano, Mulungu anayenera kuti anapanga kukonzekera kwa izo.

<sup>53</sup> Usiku wina, ndinadabwitsidwa kwambiri. Mkazi wamng’ono anadzabwera pa nsanja. Malo aakulu a madola firii handirede sauzande uko, ndipo iye anali ndi zodzipakapaka pang’ono pa nkhope yake. Iye anayima pamenepo ndipo anayamba kunjenjemera. Ine ndinati, “Ndiwe wa Lutheran,” mwa Mzimu Woyera.

Iye anati, “Inde, bwana.”

<sup>54</sup> Ndipo ine ndinati, “Inu muli pano kuti mudzapemphereredwe. Ndipo chifukwa chimene inu mukuyenda momwe inu mukuchitira, mawondo awiri onse anathyoka.” Ine ndinati, “Izo zinayambitsidwa ndi ngozi ya

galimoto, ndipo galimoto imene inu munkayendetsa, zaka foro zapitazo.”

Iye anati, “Izo nzoona.”

55 Ine ndinati, “Dokotala wanu ndi munthu wamng’ono, wamfupi, wamutu wadazi ndipo amavala magalasi.”

Anati, “Izo nzoona.”

56 Ndipo ine ndinati, “Iye akuchita udokotala chifukwa cha mu—mawondo, fupa lasanduka la chifuwa chachikulu, ndipo ngakhale mnofu ukuvunda pozungulira fupalo.”

Iye anati, “Uko nkulondola.”

Ndipo iye anati, “Kodi pali chiyembekezo kwa ine?”

57 Ine ndinati, “Izo zimatengera pa kafikiridwe kanu kwa Ambuye Yesu.” Ine ndinati. . .

Iye anati, “Kodi inu mungandithandize ine?”

58 Ine ndinati, “Ayi, amayi. Palibe amene angakuthandizeni inu tsopano. Koma inu mukuyenera kudzithandiza nokha ku madalitso operekedwa ndi Mulungu a inu.”

Ndipo iye anati, “Ine tsopano ndikukhulupirira ndi mtima wanga wonse.”

59 Ine ndinati, “Ambuye anakuchizani inu, mlongo. Ndi PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndinu wochiritsidwa.”

60 Iye anati, “Bambo Branham, ine ndakhala ndikulephera kugwada,” iye anati, “kwa zaka foro.” Akulira, atayima pamenepo, akusisita manja ake. Ndipo gulu lalikulu la anthu likulira, akumuyang’ana iye; Achilutera, Apresbateria. Ndipo ine ndinati, “Bwanji inu osapita ku guwa ndi kukagwada pansi?”

61 Iye anati, “Ndiloleni ine ndigwade pomwe apa, pomwe apa pamene ine ndachiritsidwirapo.” Iye anali asanasunthepo pa masitepe ake, koma iye amadziwa kuti wachiritsidwa. Chinachake chinachitika. Mukuona? Iye anadziwa zimenezo. Panalibe kupenekera kulikonse za izo.

Ine ndinati, “Gwadani pansi.”

62 Ndipo kwa nthawi yoyamba mu zaka foro, ndi mawondo onse awiri othyoka ndi onse owuma, anakonzedwanso, mafupa pamodzi; mkazi ameneyo, ngati mtsikana, anagwada pa mawondo ake misozi ikuyenderera mmasaya ake, anakweza manja ake kwa Mulungu. Chabwino, anangodzuka kuchoka pamenepo, mophweka basi, ngati mtsikana wamng’ono, ndi kuchoka pa nsanja. Chinali chiyani chimenecho? Mulungu anayenera kupanga njira ya izo.

63 Tsopano, Iye anatomiza madokotala, ndiko kulondola. Ndipo madokotala ndi abwino, ndipo iwo anali atachita zonse zimene iwo akanatha kuchita. Koma Mulungu anali atapanga

njira. Ndi zimenezotu. Mukuona? Dokotalayo atalephera, mu njira yake, njira ya Mulungu ndi yapamwamba kwambiri kuposa njira yathu. Ndi chinthu chopambana bwanji!

<sup>64</sup> Tsopano, kuganiza, usikuuno, kuti inu ndi ine . . . Sititero, sitikufuna kuganiza izi, koma chikhalidwe chathu ndi cha dziko lapansi, titi, ngati nkhumba. Ndipo, usikuuno, tasanduka oyera. Chinachake chimayenera kuchitika. Tsopano, ife sitingapite Kumwamba, ngati nkhumba. Ife tikuyenera kuti tipite Kumwamba, monga oyera, chotero kukonzekera kumayenera kupangidwa kwa izi.

<sup>65</sup> Ndipo Mulungu anapereka izo mokongola kwambiri mu Chipangano Chakale. Mmbuyo mu Bukhu la Numeri, pafupifupi mutu wa 20, ndi mu Eksodo pafupifupi 36, 32, ndipo ife tikupeza kuti pa Tsiku la Chitetezero . . . Mulungu, mu zoyimira, akuwonetseratu chimene Iye akanati adzachite, mwa choyimira, pamene iye anabwera, amene anali Khristu.

<sup>66</sup> Wansembe wamkulu amalamulidwa kutenga mbuzi ziwiri, mbuzi zazing’ono, ndi kuzitenga izo kuti zikhale chitetezero, nsembe, ndi ng’ombe yamphongo ya banja lake. Ndipo ambiri a inu owerenga pano, ndi owerenga Baibulo, mukudziwa momwe chitetezero chinkachitikira. Komano, mbuzi imodzi . . . Pankayenera kuti pakhale maere. Ndipo maere anagwera pa mbuzi imodzi, iyo inafa, ndiyeno magazi a mbuzi iyi amayikidwa pa mbuzi inayo, ndi manja a wansembe wamkulu, akuvomereza machimo a anthu, pa mbuzi yamoyo. Ndipo kenako munthu amene anali woyenera, amaitenga mbuzi yamoyo mmanja mwake, ndipo amapita mchipululu kumene mbuziyo inkayenera kuti ikafe ndi kupita kwa yokha, malo a kunja kwa njira. Osadzathanso, mu chikhalidwe chimenecho, kubwereranso ku banja lake lomwe, koma kukakhala kwa yokha kwanthawizonse, kunyamulira machimo a anthu kutali.

<sup>67</sup> Tsopano, ine ndikudziwa ophunzira ambiri, mwinamwake, akhala pano. Ndipo makamaka a Adventisti, iwo—iwo amanena kuti, “Mbuzi imodzi inali Khristu, ndipo inayo inali mdierekezi.” Tsopano, abale, ine ndikuyenera kuti ndisiyane pang’ono pa izo. Ife sitingathe kupereka nsembe kwa mdierekezi. Mbuzi ziwiri zonsezo zinkaimira Khristu. Ziwiri zonsezo zinali Khristu. Khristu ndi wathu . . . Iye anakhetsa magazi chifukwa cha machimo athu ndipo Iye anawanyamulira iwo kutali, Mwiniwake. Mdierekezi sanganyamule machimo anga. Khristu ndi wonyamula machimo wathu. Mumvetse izo molunjika, ndiye chikhulupiriro chanu sichisuntha. Khristu ndi wonyamula machimo wathu, ndi machimo a padziko lapansi.

<sup>68</sup> Khristu anali nyama yakufa pa mtanda, mvetserani, “Mwanawankhosa wophedwa kuchokera ku maziko a dziko lapansi.” Ndipo zoyimira zokha, ife tinkatenga zopindula, podziwa kuti choyimira chidzabwera tsiku lina.

69 Nchifukwa chiyani Iye anaphedwa kuchokera ku maziko a dziko lapansi? Chifukwa, Mulungu anazikonza mmalingaliro Ake, momwe zinthu zimenezo zikanati zidzakhali, ndi chimene mpingo ukanati udzakhale, ndi chimene chirichonse chikanati chidzakhale, ndipo Iye anayankhula Mawu. Ndipo pamene Mulungu ayankhula Mawu, izo zimakhala ngati zachitika kale, pomwe apo, chotero Iye anaphedwa kuchokera ku maziko a dziko lapansi. Inu mukuziwona izo?

70 Pamene inu mufika kwa izo tsopano, ndi kulola chikhulupiriro chanu chikhazikike mwaulemu; osati pa munthu, osati pa zaumulungu za munthu, osati pa zipembedzo za mpingo, zabwino monga izo ziri, zabwino monga munthu ali. Mulole chikhulupiriro chanu chikhale mu ntchito zotsirizidwa za Khristu pa Kalvare, za ziwiri zonse tchimo ndi chipulumutso. Inu mukuona izo?

71 Zindikirani, Khristu anabwera, ndipo Iye anali nyama yakufayo, pakuti Iye anaphedwa kale (mu fanizo) maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Inu mukuziwona izo? Mulungu anayankhula izo ndipo anati izo zikanadzakhala chomwecho. Chotero, pamene Mulungu ayankhula, izo zimatsimikiziridwa kwanthawizonse Kumwamba. Mawu, a . . .

72 Ndi pamene inu mukuyenera kukhala ndi chikhulupiriro. Ngati inu mukukhulupirira awa kuti ndi Mawu a Mulungu Amuyaya, Mawu osasinthika, ndiye langizo lililonse limene linayankhulidwa mu Mawu a Mulungu ndi Mbewu. Ndipo chirichonse chimene Mulungu wachiyankhula, mu Mawu, chinatsimikiziridwa kale mu Ulemerero. Ndipo chinaperekedwa kwa inu kuti muchitepo kanthu. Chotero musachite mantha kutenga gawo lililonse la Mawu a Muyaya, odala a Mulungu, ndi kuwazika Iwo mu mtima mwanu. Tsopano, Iwo akuyenera kukhala mu dothi.

73 Tsopano, mwa chitsanzo, ine ndatenga njere ya chimanga ndi kukaiyika iyo mu mwala wa buluu kapena chinachake monga choncho, iyo mwina siyingamere, chifukwa ndi dothi la mtundu wolakwika. Koma ngati iyo ikalowa mu dothi labwino lakuda, lachonde lapamwamba, iyo idzamera motsimikiza basi iyo ikayikidwa mmenemo. Ndipo pamene Mawu . . .

74 Ndi izi apa tsopano! Pamene Mawu a Mulungu agwera mu mtima wodzaza ndi chikhulupiriro, Iwo akungoyenera basi kuti akule. Iwo akuyenera kugwira. Ndi chifukwa chake mkaziyo atayima pamenepo, ali ndi mawondo onse okhala ndi kashiamu monga choncho, kuchokera ku zowundana, ndi kuthyoka kwa mawondo, pamene onse anaphwanyidwa, ndi mafupa atavunda ndi chifuwa chachikulu, ndiponso . . . komanso mnofu. Iye sankachita mantha kupinda mawondo ake. Kwa chiyani? Mawu anali atagwera mu chikhulupiriro. Amaphukira pamwamba! Kodi ine mukumvetsa zimenezo?

<sup>75</sup> Mulungu, maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, ananena kuti Khristu adzakhala kuno. Ndipo Iye adzapha, adzafa, wosalakwa chifukwa cha olakwa. Ndipo pamene Mulungu anayankhula izo, izo zinatsimikiziridwa kale pamene Mulungu anayankhula izo.

<sup>76</sup> Tsopano, izo zisanakhale mawu, izo zikuyenera kukhala lingaliro, pakuti mawu ndi lingaliro lofotokozedwa. Ndiyeno ngati... Mulungu, mmalingaliro Ake, anazindikira zinthu izi, pamene izo zinali mmalingaliro Ake. Zitatero, Iye anayankhula izo, ndipo zimakhala ngati kuti zinatsirizika pamene Mulungu ayankhula, chifukwa Iye ndi wosalephera ndipo sangachite china chirichonse.

<sup>77</sup> Ndiye, khalidwe la Mulungu. Ngati Mulungu anapulumutsa ochimwa kumbuyo uko, pa maziko a kulandira nsembe yopsyereza, nsembe yoperekedwa, Iye akuyenera kuti achite chinthu chomwecho lero, kapena Iye analakwitsa pamene Iye anamutengera mkati munthu woyamba ndi izo. Ngati Mulungu anachiza odwala kumbuyo uko pa maziko a magazi okhetsedwa a nyama, pa maziko a chitetezero, Iye akuyenera kuti azichita zomwezo lero, kapena Iye analakwitsa pamene Iye anachiritsa munthu woyamba. Mukuona? Iye sangathe kusintha.

<sup>78</sup> Ife timakula. Ife timakhwima. Ife timapeza zinthu zabwinoko. Ife timakamba za zinthu zabwinoko. Ife timavala zovala zabwinoko, timayendetsa galimoto yabwinoko. Ife tikupita patsogolo.

<sup>79</sup> Koma Mulungu sangapite patsogolo mwanjira imeneyo, chifukwa Iye anali wangwiro kuyamba ndi kuyamba. Ndipo ungwiro sungapite patsogolo; ndi ungwiro kale. Amen. Chotero Iye sakuyenera kunena, “Chabwino, uno ndi m’badwo wosiyana, tiri ndi lingaliro labwinoko tsopano.” Ngati ndi choncho, Iye sangakhale Mulungu. Chotero, ngati Iye ali Mulungu, chimene Iye anayankhula kumbuyo uko, Iye akuyenera kukhala ndi icho, chifukwa Iye anali wangwiro kumeneko ndipo ndi wangwiro tsopano. Mukuona? Inu mukuona izo? Ndiye, Iye sangapite patsogolo. Iye sangatero... Chabwino, ine ndikutanthauza, Iye sangazipange zinthu kukhala zabwinoko. Kuzipanga izi pang’ono... kuti, “Izi zingakhale zabwinoko pang’ono.”

Inu mukuti, “Nanga bwanji mwanawankhosa wakale, ndi Mwanawankhosa uyu?”

<sup>80</sup> Ujayu anali choyimira, kuyembekezera Iye, ndipo Iye anati iye anali. Iye anayankhula za Mwanawankhosa wophedwa kuchokera ku maziko a dziko lapansi, pachiyambi. “Ine ndidzayika udani pa Mbewu yake ndi mbewu ya serpenti.” Ndipo kenako kudikirira chidzalo cha nthawi kuja kunabwera, Mulungu anapereka chitetezero cha tchimo, kudzera mmagazi okhetsedwa a mwanawankhosa, kulozera.

<sup>81</sup> Iye anapereka chinthu chomwe chomwecho kudzera mmwezi, usiku, kukhala dzuwa masana. Mwezi pokhala mthunzi wa dzuwa, kapena dzuwa kumawalira pa mwezi, kupanga mthunzi. Mwezi ndi dzuwa ndi mwamuna ndi mkazi. Ndipo pamene dzuwa lalowa, limaponyera kuwala kwake pa mwezi, kutipatsa ife kuwala kochepea kufikira dzuwa litatuluka. Ndipo pamene dzuwa libwera, mwezi umazimirira.

<sup>82</sup> Ndipo Khristu ndi Dzuwa Limene lapita ku Ulemelero, ndi kumawalira pa Mpingo, ndi mtundu womwewo wa Kuwala kumene Iye ankawala pamene Iye anali kuno. Ndipo Mpingo ndi Kuwala kwa dziko kufikira Yesu adzabwere ndipo izo zonse zikusungunukira pamodzi. Monga kuwala kwa mwezi ndi kuwala kwa dzuwa kumakhala kuwala kumodzi, pamene zitulukira pamodzi. Ndipo pamene Khristu ndi Mpingo Wake adzabwera pamodzi, pa Zakachikwi zazikulu, adzatulukira mu chimodzi.

<sup>83</sup> Ndipo lero, “Inu ndi Kuwala kwa dziko lapansi.” Mu Kukhalapo Kwake...Mu kusowa Kwake, kani, Iye akukupatsani inu Kuwala kuti muwale nako, pamene Iye ali pano. Zinthu zonse zakale, zinthu zonse za padziko lapansi, ndi zoyimira za Kumwamba.

<sup>84</sup> Ngakhale mpaka akangaude, ndi abuluzi, ndi njoka, ndi zina zotero, ndi zoyimira chabe za mizimu yoipa, ikunyezimiritsa. Nchifukwa chiyani khansa inkatchedwa khansa? Chifukwa ili ndi mawonekedwe a nkhanu. Ndipo mawu akuti *khansa* amatanthauza “nkhanu.”

<sup>85</sup> Tsopano, inu mwaona, zinthu zonsezo zimene ziri zoyimira ndi mithunzi. Chotero, mbuzi yonamizira imene inayikidwa mchipululu, kumalo a kwa yokha, yolekanitsidwa ndi mzika zimzake, itasenza machimo a anthu pamutu pake, inali choyimira cha Khristu akulekanitsidwa kwa Mulungu, ndipo kuchoka mu Kukhalapo Kwake, ndipo atanyamula machimo athu kupita nawo ku gehena. Ndipo kumeneko Mulungu sakanamulola Iye...Davide anati, “Ine sindidzalola Woyera wanga kuti awoneke chivundi. Ngakhalenso sindidzasiya solo Yake mu gehena.” Ndipo pa tsiku lachitatu, anawukanso chifukwa cha kulungamitsidwa kwathu. Koma Iye anaifanizitsa mbuzi, mbuzi yonamizira, ndiponso mbuzi ngati nsembe ya tchimo. Mulungu akupanga kukonzekera, ndi njira yoperekedwa!

<sup>86</sup> Mulungu nthawizonse amapanga njira yothawirapo, nthawi zonse. Matenda amakuyikani inu pa kona. Satana amakukanikizirani inu pansu pa malo inu mukakhala Mkristu.

<sup>87</sup> Mwina awake mwakhala muli wa njuga. Inu mukuona zimenezo? Makadi ali pa tebulo. “Tabwera, John, ife tikudziwa izo ziri mwa iwe.” Satana ali pamenepo kuti azikuyesani inu. Koma Mulungu, iliyonse—nthawi zonse, adzapanga njira yopulumukirapo ngati inu mutangovomereza izo.

<sup>88</sup> Mwinamwake inu mwakhala muli a—chidakwa, ndipo galasi liri pansu pa mphuno yanu. “Tsopano, tabwera, John.” Tsopano, ngati inu mukufuna kumvera liwu limenero, inu mudzapita molunjika ku matope anu kachiwiri.

<sup>89</sup> Koma Mulungu nthawizonse amakhala pamenepo. Mutembenezire malingaliro anu Kumwamba, ndipo muyang’ane ku Kalvare, ndi kuti, “Mzimu Woyera wodala, bwerani kwa ine. Ine ndikusowa.” Muwone zimene ziti zichitike. Mulungu adzapanga njira yopulumukirapo, nthawi zonse, pakuti Iye adzatero. Mulungu nthawizonse wakhala akuchita zimenezo.

<sup>90</sup> Ndipo tsopano zindikirani. Dziko lapansi lisanawonongedwe, pamene anthu anali ochimwa, ndipo anthu anali ochimwa mdziko, Mulungu anakonza njira yothawirapo kwa iwo amene akufuna kuthawa nayo. Mulungu anali atamanga chombo, atachikonza. Nowa anamanga njira pa chombo kwa... kuchikonzeke retsa chombo ichi kukonzeke kwa njira. Mvetserani. Kuyambira ku... ngati njira yothawirapo, watero... Mkwiyoyi ndi chiweruzo cha Mulungu zinali zikuwunjikana mmiyamba, kuti zidzatsanuliridwe pa fuko lochimwa ndi pa anthu ochimwa, amene anakana izo, ndi owuma makosi, anayenda motsutsana ndi malamulo a Mulungu. Nthawi zonse mkwiyo uwo unali ukuwunjikana mmiyamba, kuti udzatsanuliridwe pa anthu, mu chiweruzo, Mulungu wachifundo anakonza njira yothawirapo kwa iwo akufuna kuyendamo mmenemo. Njira yothawirapo!

<sup>91</sup> Tsopano ife tafika kumalo kachiwiri amene ziweruzo zikuwunjikana. Ndipo ngati tsiku limenero, mu chigumula, ndi mochuluka bwanji lero, pamene kutha kwa mbiriyakale ya nthawi, pamene kutha kwa mbiriyakale ya mafuko, ndipo kunali kukufika pachimake! Ndi wochuluka moposa bwanji mkwiyo wa Mulungu pa mamilioni a anthu ochuluka, wawunjikana pamodzi, mpaka tchimo latsikira mu dziko, mpaka ilo likugwedezeke ngati munthu woledzera akudzandima kupita kwawo mma foro koloko. Ilo ladutsa kupyola mwezi ndi nyenyezi, mpaka ilo lafikira—zovala za Yehova wa Sabaoth.

<sup>92</sup> Ndiye, ilo likuzandima pansu pa katundu wa malingaliro ake omwe opangidwa ndi anthu, a kudzisunga kwake komwe, za zaumulungu zake zomwe. “Iwo awatenga Malamulo a Mulungu ndi kuwapanga iwo kukhala opanda mphamvu, pophunzitsa miyambo yawo yawo ya anthu. Kukonda matamando a anthu moposa matamando a Mulungu.” Aphunzitsi athu anali atakhala ofunda, ndipo akukhazikika pa kujowina mpingo, ndi kumati, “Izo ziri bwino, bola ngati inu muli wa mpingo. Mungoyiwala za izo.”

<sup>93</sup> Koma, m’bale, Mulungu anakonza njira yothawirapo. Ndipo inu mudzayenera kufika ku zofuna za Mulungu, ndipo ndizo kudzera mwa Khristu Yesu Ambuye wathu. Palibe maziko ena



ayikidwa koma amene anayikidwa kale, ayi, palibe amodzi. Kumanga pa maziko ena aliwonse, kuli ngati ziputu ndi matope, madzi osefukira adzakokolola izo, ndipo kugwako kudzakhala kwakukulu. Koma Yesu anati, “Pa thanthwe ili, Ine ndidzangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzawulaka Iwo.” Ndi chiyani chimene Iye anamangapo Iwo? Pa Choonadi chowululidwa chاوزimu kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu.

“Kodi anthu amati Ine Mwana wa munthu ndine yani?”

<sup>94</sup> “Ena amati ‘Eliya,’ ndipo ena amati ‘Mose,’ ndipo ena amati ‘Yohane M’batizi,’ ndi zina zotero.”

“Koma inu mumati Ine ndi ndani?”

<sup>95</sup> Mopanda kukayikira, popanda kutenga mphindi... Mvetserani, wochimwa. Umo ndi momwe inu mumalandirira izo. Iye anakhala ndi Iye; iye ankadziwa chimene Iye anali. Ndipo kenako iye asanaganize nkomwe kachiwiri, Mzimu Woyera unamugwira iye, ndipo iye anati, “Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo.”

<sup>96</sup> Anati, “Iwe, wodala ndi iwe Simoni, Simoni Bar-yona, pakuti thupi ndi mwazi sizinawululire izi kwa iwe. Iwe sunaphunzire izi ku zaumulungu za winawake. Iwe sunabwere kuchokera ku seminare ndi izo. Koma Atate Anga Amene ali Kumwamba awulula izi kwa iwe. Pa thanthwe ili, Ine ndidzangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzawulaka Iwo.”

<sup>97</sup> Kusefukira kukhoza kubwera, ndipo ma atomiki akhoza kugwa, ndi zonse, koma iye amene ali wotetezedwa mwa Khristu adzakwera mkuntho wa atomiki, chimodzimodzi monga anachitira Nowa ndi namondwe wa kusefukira, wotetezeka mu chombo. Mulole chikhulupiriro chanu chigwere mu zimenezo, kamodzi, muwone chimene chitachitike; pa thanthwe lolimba la Mulungu, pa zoyimira. Mulungu amakonza njira yothawirapo, nthawi iliyonse. Iye amayenera kukonza njira yothawirapo. Pamene nthawi yoikika ifika, Mulungu ndi Mulungu. . .

<sup>98</sup> Yehova-yire! *Yehova-yire* amatanthauza, “Yehova adzapereka Iyemwini nsembe,” pakuti Ambuye adzazikonzera Yekha njira yothawirapo. Mulungu akhoza kupereka iyo chifukwa Iye ndi Mlengi. Ndipo Mulungu, kamodzi kwa zonse, pa Kalvare! Amen! Uko, kumeneko pamene Angelo aakulu a Kumwamba, pamene makamu onse a ziwanda ananjenjemera, pamene dziko lapansi linadzilambatitsa ndi manjenje ndi kugwedeza manda, ndipo pamene dzuwa linagwedezeka ndipo linapachikika mmbuyo uko, ndipo linasanduka mdima, pamene mwezi ndi nyenyezi zinagwedezeka kuchoka pamalo awo, owomboledwa a mibadwo yonse, ndipo kupyola mu mibadwo adzabwera, adzazindikira ora limenero.

<sup>99</sup> Pamene Mwana wa Mulungu anafa pamenepo, anamulanda Satana mphamvu iliyonse. Ngakhale imfa, ndi gehena, manda, ndi mantha onse, zinamezedwa pamenepo pa Kalvare. Pamene Iye analipira mtengo wapamwamba ndi pamene Mwanawankhosa anafa, ndipo machimo anayikidwa pa Iye, Iye anali wonyamula tchimo, anawatengera iwo ku gehena kumene kunali kwawo. Ndipo Mulungu anamuukitsa Iye tsiku lachitatu. Ndipo pokhulupirira zimenezo, ife timalungamitsidwa mwa chikhulupiriro, pa maziko a Magazi okhetsedwa a Ambuye Yesu Khristu. Amen. Mulungu kupanga njira yothawirapo.

<sup>100</sup> Oh, m'bale, pamene inu muwona...mumva ambulansi ikulira, nthawi iliyonse mukamva imodzi, ndi chizindikiro chakuti mukupita njira imeneyo. Nthawi iliyonse mukamadutsa pa manda, ndi chizindikiro. Inu mukupita njira imeneyo. Nthawi iliyonse makwinya awonekera pa nkhope, ndi imvi mmutu, ndi chizindikiro. Inu mukupita njira imeneyo.

<sup>101</sup> Nzosadabwitsa, ndiye, Paulo akanatha kunena, ndi chiyembekezo chenichenicho chimenecho chozikika ndi chozikika mwa iye, monga chonchi. Mai! Pamene iye anafika kumapeto kwa msewu, iye anati, "Ndamenya nkondo yabwino. Ndamaliza ntchitoyo. Ndasunga chikhulupiriro. Kuyambira tsopano, kwayikidwa kwa ine korona wa chirungamo, Ambuye Woweruza wolungama adzandipatsa ine pa tsiku limenero, osati ine ndekha, koma onse amene amakonda kuwonekera Kwake."

<sup>102</sup> Pamene inu mudwala ndi kutopa ndi moyo wakale uno, ndipo inu mudzakukonda kuwonekera kwa Ambuye Yesu mwabwino kuposa momwe inu mumakondera chakudya chanu pa tebulo, kapena akazi anu, kapena ana anu, ndiye pali korona woyikidwiratu kwa inu. Osati korona, korona wagolide woti adzayikidwe pamutu panu. Koma thupi, lopanda zowawa, a...litavekedwa korona mu Ulemelero wa Mulungu, litavekedwa korona mu chisavundi cha Yesu Khristu. Ndi chimene chayikidwa kwa inu, chimene Ambuye, Woweruza wolungama adzakupatsani inu pa tsiku limenero. Ndiro tsiku limene tikuliyembekezera. Mulungu wakonza njira yothawirapo kwa aliyense wa ife. Ndithudi Iye watero.

<sup>103</sup> Pamene Daniele mneneri, mwana wa Mulungu, anaponyedwa mu dzenje la mikango. Inalipo nthawi imene Daniele, pokhala wokhulupirika, amene anakweza mazenera ake ndipo sanachite mantha ndi chimene mfumu inanena. Ndipo pamene a...anapemphera, mosasamala kanthu za cholengeza chimene chinalengezedwa, Daniele anapemphera mulimonse, pamene iye ankayang'ana ku Yerusalemu ndi kupemphera. Ngati anthu ankayang'ana ku Yerusalemu ndi kumapemphera, mzinda umene nsembe yopsyereza inkaperekedwako...Ndi chifukwa chake Daniele ankayang'ana mbali imeneyo ndipo anapemphera, pakuti Ambuye anali atanena kale, "Anthu akadzakhala mu vuto nthawi iliyonse, ndipo akadzayang'ana

ku malo oyera awa, ndi kupemphera, ndiye mudzawamve . . . Ine ndidzamva kuchokera Kumwamba,” pamene Solomoni ankampereka kachisi.

<sup>104</sup> Ndi chifukwa chake Yona anali ndi chikhulupiriro chimene iye anali nacho, pamene iye anali ndi udzu wa mnyanja utakulungidwa pakhosi pake, ndipo akuyima mu masanzi, mmimba mwa chinsomba, komwe mu kuya kwa nyanja, pa nyanja ya mkuntho. Iye anati, “Izo ndi zachabechabe zabodza. Koma kamodzinso ndidzayang’ana ku Kachisi wanu woyera, Mulungu.” Mulungu anachita chinachake. Iye anapanga njira yothawirapo kwa Yona. Chimene Iye anachita, palibe amene akudziwa. Icho ndi chinsinsi cha Mulungu mwini.

<sup>105</sup> Koma, mosasamala pamene zinali zosatheka, Mulungu akhoza—akhoza kusintha zochitika. Iye akhoza kupanga chosatheka kukhala chotheke. Ndipo osati chotheke chokha, koma akhoza kupanga izo kukhala chenicheni, pamene anthu amutenga Mulungu pa Mawu Ake ndi kuvomereza njira yoperekedwa imene Mulungu anaipereka kwa munthu.

<sup>106</sup> Mulungu anachita chinachake. Iye mwina anayika hema wa mpweya pansi apo. Ine sindikudziwa chimene Iye anachita mmimba mwa chinsomba chimenecho, koma Iye anamusunga Yona mmenemo kwa masiku atatu ndi usiku, monga choyimira, kuti Khristu adzagona mopanda mpweya, mmimba ya dziko lapansi, ndipo pa tsiku lachitatu Iye adzatulukamonso. Icho chinali choyimira. Iye anapanga njira yopulumukira. Iye nthawizonse adzatero.

<sup>107</sup> Pamene Daniele anayima pamenepo, ndipo mikango ikubwera, ikuthamangira kwa iye, munalibe nkomwe mantha mu mtima wa woyera wokalambayo. Koma iye anayima pamenepo, ndipo Mulungu anali asanathane naye iye. Ndipo mikangoyo itangotsala pang’ono kumugwira iye, Mngelo anatambasula pamaso pa iyo, mosakayika koma Kuwala koyaka komweko kumene kunawonekera kwa Saulo wa ku Tariso, panjira ya ku Damasiko.

<sup>108</sup> Kuwala kwakukulu kunawala. Ndipo iwo anayang’ana, ndipo iwo sanadziwe chimene chinkachitika. Ndipo Saulo anagwa pa kavalo wake. Ndipo Liwu linadza kuchokera mu Kuwalako, likuti, “Saulo, Saulo, nchifukwa chiyani iwe ukundizunza Ine?”

Anati, “Ndinu ndani, Ambuye?”

Iye anati, “Ine, Yesu, amene iwe ukumuzunza.”

<sup>109</sup> Anali ana Achihebri amene anali okhulupirika ku lonjezo la Mulungu, amene anali atakhala pansi umo mu ng’anjo ya moto . . . kapena mu Babeloni, kani, akupita ku ng’anjo ya moto. Sitepe imodzi pakati pa iwo ndi imfa.

<sup>110</sup> Zingakhale zochuluka bwanji kwa amuna pano usikuuno. Pakhoza kudzakhala tsiku limodzi pakati pa inu ndi kulekana Kwamuyaya. Inu mudzapanga chisankho chanu tsopano. Njira yaperekedwa kwa inu ngati inu mungayivomere iyo. “Sitepe imodzi,” anatero Yonatani kwa Davide, pamene iwo anawombera a—a—uta, “sitepe imodzi pakati pa ine ndi imfa.”

<sup>111</sup> Ndipo sitepe imodzi pakati pa iwo ndi imfa. Koma basi pa nthawi yovutayo, Mulungu anapereka njira yothawirapo, ndipo Iye anatumiza mu ng’ango yamoto ija Ambuye Yesu Khristu, ndipo anazimitsa moto kwa iwo.

<sup>112</sup> Anali Enoki, amene ankadzinenera kuti anayenda ndi Mulungu kwa zaka faivi handirede ndipo anali ndi umboni iye “anamukondweretsa Mulungu.” Iye anali ndi chikhulupiriro kuti iye “sadzawona imfa.” Mulungu akanakhoza bwanji kuchita zimenezo? Panalibe ngakhale ndege ya jeti mmasiku amenewo, kuti imuchotse iye pa mapazi ake. Koma Mulungu anapereka njira, kusanthulika, kumene kunamuchotsa Enoki pa dziko lapansi kupita ku Ulemelero, popanda kulandira imfa.

<sup>113</sup> Anali Eliya amene anaponda pa nyanja . . . kapena mtsinje wa Yorodano tsiku limenero, pogawaniza iwo kuchokera mbali imodzi kupita ku ina. Ndipo pamene Eliya anali atakonzeka kuti azipita Kumwamba, wopanda kufa, anali Mulungu anapereka njira kwa iye. Osati ndege ya jeti, koma Iye anatumiza galeta wa Moto, woyendetsedwa ndi akavalo a Moto. Mulungu anapereka njira, mu miniti, njira yothawirapo ku imfa.

<sup>114</sup> Anali Mose, ine ndikukhulupirira, amene anawatsatira ana a Israeli . . . kapena amene anawatsogolera iwo, akutsatira Kuwala, Lawi la Moto, kudutsa mchipululu. Anali Mose amene anapirira mpaka kumapeto. Anali Mose, zaka handirede ndi twente, zitatha zaka eyite za utumiki kwa Mulungu, amene anayima pa phiri ndipo anayang’ana mu dziko lolonjzedwa, ndi misonzi ikuyenderera pansu pamasaya ake, bambo wachikulire, wa usinkhu wa zaka handirede ndi twente. Iye anali atabwera kudutsa njira za minga. Iye anali atayenda mmadzi akuya. Iye anali atalawa chikho chowawa, chikho cha ndulu ndi chisoni. Iye anakhala ndi anthu osamvera, ngati m’busa wawo. Iye anali atawatsogolera iwo kuchoka kumalo kupita kumalo, ndipo anapirira ndi kung’ung’udza kwawo. Ndipo anadziponyera yekha pa cholekanitsa, ndipo anati, “Mulungu, munditenge ine Inu musanawatenge iwo.”

<sup>115</sup> Anali Mose amene anaimea pamenepo, ngati bambo wokalamba, akudziwa kuti mu njira iliyonse anali choyimira cha Khristu, akudziwa mwinamwake, mwanjira ina, Mulungu ndithudi akanadzamutenga iye, chifukwa Iye ankayenera kuti adzamubweretsenso iye, ngati choyimira cha Khristu. Iye anabadwa monga mneneri, monga Khristu. Ndipo osati kokha mneneri, koma mtsogoleri, ndi zina zotero. Iye anakabisidwa

kutali mu tchire, ndipo chomwechonso Khristu anatengedwera kupita ku Igupto. Iye anali wopereka malamulo, monga Khristu anali ku phiri la Azitona, amene ankakhala ku Sinai. Njira iliyonse, iye anali choyimira cha Khristu.

<sup>116</sup> Ndipo pamene iye anakalamba, ndipo imfa ikumuyang'ana iye pa nkhope, iye akanabweretsa bwanji chiukitsiro? Koma pamene nthawi yovuta inafika, Mulungu anapereka njira. Pamene mpweya unkamuchokera, ndi kumagwedeza pakhosi pake, iye anayang'ana, atagona pambali pake, ndipo apo panayima Thanthwe. Mulungu anapereka Thanthwe. Thanthwelo linali Khristu Yesu amene anali mchipululu. Mose anapirira Thanthwe.

<sup>117</sup> Mulungu, ndipatseni ine chisomo kuti ndipirire ku chinthu chomwecho. Ndipo pamene mpweya wa moyo wanga udzachotsedwa kuchoka mu thupi ili, ndiloleni ine ndidzawone Thanthwelo litayima pamenepo.

<sup>118</sup> Anaponda pa Thanthwelo, ndipo Angelo anabwera ndipo anadzamunyamulira iye kutali. Zaka eyiti handiredede mtsogolo, iye anali atayima ku Palestina, ndi Eliya, atayima pamenepo akuyankhula ndi Yesu, mtanda usanati. Mulungu anakonza njira yothawirapo.

<sup>119</sup> Ziwiri mwa zinthu zazikulu mu Chipangano Chakale, zimene ine ndikutha kuziwona mu mauneneri, magulu awiri aakulu, zinali izi. Anthu ankayembekezera nthawi kufikira pamene Mesiya adzabwere. Ndiyeno, Mesiya atabwera, iwo ankayembekezera nthawi, imene Mzimu Woyera ukanati udzabwere.

<sup>120</sup> Potsiriza, mu nthawi yake, zoyimira zonse kumbuyo uko, zomwe iwo anali nazo kupyolera mwa aneneri ndi chirichonse, zoyimira zonse ndi zitetezero zimene iwo anali nazo, potsiriza Mesiya anadzabwera, ndipo izo zinakhazikika chifukwa Mulungu anali atanena chomwecho.

<sup>121</sup> Ndiye iwo ankayembekezera nthawi, ku “Mpingo waukulu waulemlero umene udzakhale wopanda banga kapena khwinya,” umene udzawale padziko lapansi ngati nyenyezi. Iwo ankayembekezera nthawi imeneyo. Kodi izo zidzakhala motani? Iye anali atafa kwa masiku atatu ndi usiku. Iye anawukanso. Iye anawonekera kwa faivi handiredede, ndipo Iye anakwera Kumwamba. Iye anawasiya iwo pa dziko pano, okha. Ukhala bwanji Mpingo waulemlero uwu, pamene Mtsogoleri wapita? Mulungu anawulonjeza Mpingo. Zikanadzakhala motani Kuwala kumene kukanadzawala mmalo Ake, Iye atachoka kale?

<sup>122</sup> Pamene Iye ananena pamenepo, “Kanthawi pang'ono, ndipo dziko silidzandiwonanso Ine; komabe inu muzidzandiwona Ine, pakuti Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumapeto a dziko lapansi. Zinthu zimene Ine

ndikuchitazi inunso mudzazichita. Pitani inu mdziko lonse ndipo mukalalikire Uthenga. Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.”

<sup>123</sup> Iwo angachite motani izo, Khristu kulibeko kwa iwo? Iwo angachite bwanji izo, pamene Mulungu anawapatsa iwo lonjezo? Koma, taonani, Mulungu anapereka pentekoste, pamene Mzimu Woyera, mwa Munthu, unatsika pansu ndi kudzatenga thupi la munthu wachivundi iwo atatha kuyeretsedwa ndi Chitetezero cha Ambuye Yesu Khristu. Ndipo Mzimu Woyera unamutengera munthu ameneyo mu ulamuliro Wake womwe, ndipo unamutumiza iye ndi zizindikiro ndi zodabwitsa ndi zozizwitsa zikumutsatira. Mulungu anapereka njira. Iwo sakanakhoza kuchita izo mwa iwookha. Iwo anali amuna ngati inu ndi ine. Kodi iwo akanachita bwanji izo? Iwo sakanakhoza. Koma Mulungu anapereka njira yothawirapo.

<sup>124</sup> Pamene iwo anali . . . ? . . . mu chipinda chapamwamba, iwo ankaganiza kuti anthu akanawaseka iwo. Iwo ankaganiza kuti iwo akanadzakhala *ichi*, *icho*, kapena *chinacho*. Iwo anatseka mazenera onse, ndi kukhoma zitseko. Kodi iwo achita bwanji izo? Iwo anali amantha. Iwo analibe fupa la pansana. Iwo anali ndi ndi nsana wa nkuku, ndipo osati kwenikweni nsana wa Mzimu Woyera. Iwo anali atatseka zitseko. Iwo ankachita mantha. Iwo ankachita manyazi kuti atuluke ndi kukayang'anizana ndi anthu. Kodi iwo akanachita bwanji izo?

<sup>125</sup> Koma Mulungu anatumiza pentekoste, ubatizo wa Mzimu Woyera. Iwo anakankha mazenera ndi kutsegula zitseko, ndipo anapita mmisewu. Mulungu analonjeza izo. Pamene Mulungu walonjeza, Mulungu amasunga Mawu Ake. Iye amapanga njira yothawirapo. Iye sadzakulolani inu kuti muyesedwe pamwamba pa chirichonse chimene Iye sangakupangireni njira yothawirapo. Iye adzachita izo.

<sup>126</sup> Ndi ife pano, takhala kudutsa mu tsiku la chimbuuzi, lamitambo, lamvula. Mpingo uli theka mkati ndi theka kunja. Iwo akudabwa momwe angachitire *ichi*, ndi momwe angachitire? Iwo analibe Kuwala. Koma mneneri anati, “Kudzakhala Kuwala mu nthawi yakumadzulo.” Izo zingatheke bwanji? Ife ta . . . Mpingo mu tsiku lino, Mpingo waulemelero umenewo umene uti udzakhale kuno pa dziko lapansi, pamene Yesu adzabwera kuti adzawulandire Mpingo waulemelero, ife tikulandira mvula ya masika, kutsanulira. Magawo awiri a Mzimu Woyera akubwera pa dziko lapansi, ndipo akusesa fuko lirilonse, ndipo moto wa chitsitsimutso ukuyaka pa mapiri aliwonse. Ku China, ku Japan, kuchokera ku Korea, Afrika wa mdima, ndi kulikonse, Mzimu Woyera ukutsanuliridwa pa anthu. Mulungu anapanga njira.

<sup>127</sup> Kodi maso anga akhungu anachiritsidwa bwanji? Mulungu anapanga njira. Aleluya! Inde, bwana.

128 Iye nthawizonse amapanga njira. Ndipo kwa inu pano, amene muli padziko lapansi lero, inu amene mukuyembekezera chithonhozo, inu amene muli amwendamnjira ndi alendo, mukhale ngati Davide.

129 Davide ankapita ku nkondo. Iye sanapite wokhumudwa. Iye sanapite ndi chizindikiro cha theka. Iye sanapite akuganiza kuti mwina izo zichita izo. Koma iye anadikirira mu chitsamba cha mabulosi mpaka, patapita kanthawi, kunali chete, panalibe chimene chinkachitika. Patapita kanthawi, kumbuyo cha patali, iye anamva masamba akuyambapo, amamveka mokuwa ndi mokuwa ndi mokuwa. Patapita kanthawi, mphepo yamkuntho inapita patsogolo pake. Iye anadziwa kuti ameneyo anali Mulungu ndi khamu loyera la Angelo likupita patsogolo pake. Ndipo iye anasolola lupanga lake, ndipo anatenga nkondoyo, ndipo anamupangitsa mdani kuthawa.

130 M'bale, musamalumphe ndi kuganiza chinachake pamene simuli woyenera kuti mupite. Muziima! Ndipo muwone kuti si kujowina tchalitchi, osati kugwirana chanza ndi mlaliki, komanso si kubatizidwa mmadzi. Koma ndi kulandira nsembe yoperekedwa ndi Mulungu, Yesu Khristu, monga Munthu mu mtima mwanu. Mzimu Woyera udzasunthira patsogolo panu, monga mphepo ya mkokomo, ikusunthira chirichonse kuchoka panjirapo. Amen. Ndi zimenezotu. Ndiye, khalani Akhristu. Inu amene muli mnjira, mukhale amuna enieni owopa Mulungu.

131 Kukubwera chitsitsimutso kuno, posakhalitsapa, msonkhano wawukulu wamu hema. Ine ndikukhoza kuwuwona iwo. Kulondola! Kodi inu mukufuna kuchita chiyani? Mudzikhaliitse nokha wa khalidwe . . .

132 Kuno nthawi ina kale, uko ku mayiko akummwera, kunali anthu amene anakakonda kudutsa ndi kugula akapolo, ndi zina zotero. Ine ndinangopezeka ndikuganiza za nkhani yaying'ono iyi. Pamene iwo ankadutsa, ankgula akapolo, iwo anakawona kuti anthu osaukawo amenyedwa. Iwo anakadana nazo kuti alisiye dziko lawo, ndipo iwo ankadziwa kuti sadzabwereranso. Anthu Achikuda, zinali zomvetisa chisoni mmene iwo ankachitidwira.

133 Tsiku lina iwo anamzindikira mnyamata mmodzi mapewa ake ali mmbuyo. Iwo sankasowa kuti azichita kumumenya iye. Ayi, bwana. Wogula wina anabwera, anati, "Ndiloleni ine ndigile kapolo ameneyo."

Iye anati, "Iye si wamalonda."

134 Iye anati, "Chabwino, nchiyani chikumupanga iye kukhala wosiyana kwambiri? Kodi iye ndi bwana pa ena onsewo?"

Anati, "Ayi."

135 Anati, "Nchiyani chikumupangitsa iye kukhala wosiyana? Kodi mumamulola kuti azidya bwinoko?"

Anati, “Ayi. Iye amadya ndi ena onsewo.”

Anati, “Nchiyani chikumupangitsa iye kukhala wosiyana kwambiri?”

<sup>136</sup> Anati, “Ndinamva kuti abambo ake ndi mfumu ya fuko. Ngakhale iye ali kudziko lakutali, iye amagwetserabe mapewa ake mmbuyo. Iye ndi munthu wobadwa mwachifumu. Abambo ake ndi mfumu. Ngakhale kuti iye ndi mlendo, abambo ake ndi mfumu.”

Bambo anga ndi wolemera ali nazo nyumba ndi minda,  
Iye amagwirizira chuma cha dziko lapansi mu dzanja Lake!  
Cha miyala yodula ndi madaimondi, ndi siliva ndi golide,  
Nkhokwe zake ndi zodzaza, Iye ali ndi chuma chosaneneka.

<sup>137</sup> Ife, anthu pano pa kachisi uyu, tiri ndi umboni wosalephera wa Ambuye Yesu woukitsidwayo, ndi chitsitsimutso chimene chasesa dziko; kuchokera ku malo aang’ono odzichepetsa monga awa, osaposa modyera ng’ombe ku Betelehemu, ndipo mwinamwake odzichepetsa kwambiri. Koma kudzera pano, Mulungu watumiza chitsitsimutso chachikulu, wasesa ma teni a masauzande, inde, kufika mamiliyoni, kulowa mu Ufumu wa Mulungu.

<sup>138</sup> Kodi inu mukufuna kukhala nzika imzathu ndi ife? Kodi ndinu okonzeka usikuuno, wochimwa, kuti muponyere pansu kusayanjanitsika kwanu, kuponyera pansu moyo wanu wochimwa? Ndi kuwongola mapewa anu ndi kujowina gulu la ankhondo ili, la anthu oguba, kukhulupirira kuti Chitetezero cha Ambuye Yesu Khristu chimatiyeretsa ife ku tchimo lonse.

Tiyeni tipemphere, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu.

<sup>139</sup> Atate athu Akumwamba achifundo, usikuuno, pamene ife tikuyembekezera pa Inu, kuyembekezera Mzimu Woyera wawukulu wa Mulungu kuti usunthe kudutsa mwa omvetsera awa ndi kuchita mopitirira zochuluka. Monga takonzekera tsopano, pa usiku wolowa mchaka china kuti titenge mgonero, O Atate Mulungu, ife tikupemphera kuti Inu muyankhule ku mitima ya ochimwa, usikuuno. Aloleni iwo abwere, Ambuye, mophweka osati motengeka, osati ndi nkhani ina yachisoni, koma moonadi pa Mawu osaipitsidwa a Mulungu. “Kuti Mulungu anakonda dziko lapansi, Iye anampereka Mwana Wake yekhayo wobadwa yekha, kuti aliyense amene akhulupirira mwa Iye asatayike koma akhale nawo Moyo Wamuyaya.”

<sup>140</sup> Mulungu, perekani, usikuuno, kuti Mawu a Ambuye Yesu, mu Yohane Woyera 5:24, amveke mu mtima uliwonse. “Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha, ndipo sadzabwera mu chiweruzo,



koma wadutsa kuchoka ku imfa wapita ku Moyo.” Mulole ambiri adutse, ora lino, achoke ku imfa apite ku Moyo, pamene ife tikuyembekezera Mzimu Woyera, kudzera mu Dzina la Yesu Khristu.

<sup>141</sup> Ndipo ndi mitu yanu yoweramitsidwa. Ine ndikudabwa, pamene mlongo akuyimba, ngati... Aliyense, Mkhristu, mu pemphero. Kodi alipo mwamuna, mkazi, mnyamata, kapena mtsikana, amene mungakweze dzanja lanu kwa Mulungu? Osati kwa ine. Ndikuti, “Apa... Ine ndikukweza dzanja langa, kuti ndinene kwa Inu, Mulungu, ine ndikukhulupirira kuti chiweruzo chakonzeka kuti chikanthe dziko lapansi. Ndipo ine ndiri pansu pa kutsutsidwa kwa chiweruzo ichi. Ine ndiyenera kulekanitsidwa ndi Mulungu, kuchoka pamaso pa Mpingo, kuchoka pamaso pa anthu Achikhristu. Ine ndikuyenera kuzunzidwa kwanthawizonse, mu gehena Yamuyaya. Koma, usikuuno, ine ndikumverera Mzimu Wanu ukuyankhula kwa ine, kuti ine ndikuyenera kusankhidwa ndi Mulungu. Pakuti, Yesu anati, ‘Palibe munthu angabwere kwa Ine, pokhapokha Atate atamukoka iye.’ Ndipo ine ndikumverera kukoka kwachirendo mu mtima mwanga, mwakuti tsopano ndikufuna kumulandira Khristu ngati Mpulumutsi wanga. Ndipo, Mulungu, ine ndikukwezera dzanja langa kwa Inu, ndi kunena, kwa izi, ine tsopano ndikumuvomereza Mwana Wanu, Yesu Khristu, Nsembe yanu yoperekedwa, chifukwa cha machimo anga oyipa ndi a mbiri-yoyipa. Ine tsopano ndikukwezera manja anga kwa Inu.” Kodi inu muchita izo?

<sup>142</sup> Mwamuna kapena mkazi, mnyamata kapena mtsikana, muno, pa nthawi ino, mungakweze mmwamba manja anu ndi kunena, “Ndi ichi, ine tsopano ndikumulandira Ambuye Yesu Khristu ngati Mpulumutsi wanga.” Ndikudikirira mphindi kuti mupange chisankho chanu. Mungokweza dzanja lanu. Mulungu akudalitseni inu, mnyamata wamng’ono. Winawake kwezani dzanja lanu, nenani... Mulungu akudalitseni inu, m’bale wanga. Chabwino. Inu mukupanga izo kwa Mulungu, osati kwa ine.

<sup>143</sup> “Onse amene anakhulupirira anabatizidwa, ndipo anawonjzedwa ku mpingo.” Miyoyo firii sauzande inapulumutsidwa.

Pali kasupe wodzazidwa ndi Magazi,

<sup>144</sup> Ndithudi. Kodi inu mungagwere tsopano, mwa chikhulupiriro, mukuti, “Ambuye Mulungu, ine tsopano ndazidula. Oh, ine ndapitapo ku guwa, nthawi zambiri. Ine ndachitapo *ichi*, *icho*, kapena ine ndajowinapo tchalitchi. Ine ndayeserapo kuthawa mkwiyo. Koma, usikuuno, ine ndikubwera njira iyi, pa maziko a Yesu Khristu kufa mmalo mwanga, Iye anali Mwanawankhosa woperekedwa nsembe. Iye anali mbuzi yothawirapo. Iye anali zonse. Ndipo, mwa Iye, ine ndi wamphumphu. Iye ananyamula machimo anga. Iye anatenga

malo anga pa Kalvare. Iye anatenga malo anga pansi pa mkwiyo wa Mulungu. Iye anatenga malo anga pansi pa chilango cha Mulungu. Iye anatenga malo anga mu gehena. Ndipo kuti ine nditenge malo Ake Kumwamba, kuti ndidzakhale mwana wa Mulungu, ine tsopano ndikuvomereza maziko amenewo pakali pano. Monga wochimwa, ine ndikukhulupirira.” [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

Pamene ochimwa agwera mmadzi osefukira,  
Ataya madontho awo a zolakwa.  
Ataya zawo zonse . . .

<sup>145</sup> Mukhale mu pemphero, mpingo, pamene winawake akupanga lingaliro kwa Ambuye. Pempherani. Ataya zingati? Madontho awo onse a zolakwa. Myuda, Wamitundu, kapolo kapena mfulu, wochimwa kapena membala wa mpingo, wansembe, dokotala, woyimira milandu, chirichonse chimene inu mungakhale, kutaya dontho lanu lonse la zolakwa, pa kukhulupirira pa Ambuye Yesu, mulandireni Iye ngati Mpulumutsi wanu. Mvetserani ku ndime iyi, pamene ife tikuyimba mwakachetechete tsopano.

Wakuba pa kufa anasangalala kuwona  
Kasupe ameneyo . . .

<sup>146</sup> Pamapeto a msewu, ziyembekezo zonse zitapita, apo panawonekera Kasupe. Kodi inu muli kumapeto, usikuuno, kwa chifuniro chanu chomwe?

Ochimwa akagwetsedwera mkati . . .  
Ataya dontho lawo lonse la zolakwitsa.  
Ataya dontho lawo lonse la zolakwitsa,  
Ataya . . .

<sup>147</sup> Tsopano, Atate Akumwamba, izo zonse ziri mmanja Mwanu. Bambo wachikulire ndi mnyamata anakweza manja awo, kuti iwo akufuna kuti akulandireni Inu, pamene Kasupe watsegulidwa kupyolera mu Mawu. Ife tikuyamikira chiyanjano Chanu, Ambuye, Mzimu Woyera.

<sup>148</sup> Mwinamwake iwo onse ndi Akhristu, onse otetezeka. Inu mukudziwa mitima yawo, Ambuye. Iwo mwina anawoloka ngakhale mzere wa pakati pa chifundo ndi chiweruzo, osafunanso kuti akweze dzanja lawo, kapena osafunanso kukhala ndi kumverera kulikonse kuti Inu mungawayitane iwo. Ine ndikupemphera, Atate, ngati izo ziri chomwecho, tichitireni chifundo.

<sup>149</sup> Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu mumupulumutse bambo uyu, Ambuye. Ine ndikupemphera kuti pakali pano, pansi mu mtima mwake, mabelu achisangalalo a Kumwamba akulira. Ndipo mnyamata wamng’ono uyo, mwanjira yomweyo. Podziwa ichi, kuti Yesu ananena mawu awa, “Iye amene amva Mawu Anga, nakhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha, ndipo sadzabwera konse ku chiweruzo, koma

wadutsa kuchoka ku imfa kupita ku Moyo.” Amenewo ndi Mawu Anu, Atate, ndipo ife tikuwakhulupirira Iwo. Apatseni iwo chimwemwe chosatha tsopano, kuti iwo alandira Moyo wosatha. Ife tikupemphera, kuti Inu mupangitse moyo wawo kudzaza ndi chimwemwe, ndi wopindulitsa ndi chisangalalo. Perekani izi, Ambuye.

<sup>150</sup> Adalitseni ena, pamene ife tikuyembekezera pa Inu, mu Dzina la Yesu ife tikupemphera. Amenii.



*KUPANGA NJIRA* CHA56-0304  
(Making A Way)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lamlungu madzulo, Marichi 4, 1956, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2023 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)